# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA MANGOCHI M'DZINJA LA 2025-2026

## Nyengo ya dzinja ya 2025/2026 mwachidule

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/26.


Boma la Mangochi likuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo.

## October 2025





Madera ambiri m'bomali kudzakhala kopanda mvula mu mweziwu. Komabe, madela ena akuyembekezeka kulandila mvula ya chizimalupya ya mphepo yankuntho yosaposera 30mm.

## November 2025




Madera ambiri akhoza kudzalandira Mvula ya mlingo wa pakati pa 30mm ndi 100mm omwe uli mlingo ochepela okhazikika.

## December 2025





Mu December, madera ambiri akuyembekezeka kulandila mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm ndi 200mm.

Mvula ya mphezi ndi mphepo ya mkutho ikuyembekezeka.

Mvula yokhazikika yikuyembekezeka kuyamba m'sabata yachitatu ya mwezi wa December.

## January 2026





Mwezi wa January ukuyembekezeka kukhala wa chinyontho chochuluka.

Madera ambiri a kwa TA Nankumba, SC Namabvi, TA Jalasi, SC Chowe, and SC Mbwana Nyambi akuyembekezeka kulandila mlingo wa mvula wa pakati pa 250–300 mm.

Ng'amba yofika sabata imodzi ikuyembekezeka mu mweziwu.


## February 2026




Mlingo wa mvula yokhazikika kapena kuchepera apo ikuyembekezeka m'madera ambiri. Mlingo wa mvula wa pakati pa 200-250mm ikuyembekezeka madera ambiri.


Pali chiopsyezo cha ng'amba ya sabata imodzi mu mweziwu.

## March 2026




M'mweziwu boma la Mangochi likuyembekezeka kulandila mvula ya mlingo okhazikika kapena kuchepela apo yapakati pa mlingo wa 150-200mm.

## April 2026





Mlingo wa mvula yochepera 50mm, ukuyembekezeka mu mweziwu m'madera ambiri.

Nyengo yadzinja ikuyembekezeka kufika kumapeto mu sabata loyamba m'mweziwu.

Boma la Mangochi ikuyembekezeka kulandila mvula yya mlingo wokhazikika kapena kuposela apo mu dzinja la 2025/2026. Mvula yokhgazikika ikuyembekezeka kuyamba sabata lachiwiri la mwezi wa December.Nyengo ya mvula ikuyembekezeka kufika kumapeto sabata loyamba la mwezi wa April chaka cha 2026. Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kukhala yotali masiku a pakati pa 120 ndi 130. Pali chiopsezo cha ng'amba ya sabata imodzi mwezi wa January ndi february m'chaka cha 2026.

*Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi yaperekedwa m'munsimu.*

| MANGOCHI | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 3.0 | 20.5 | 11.6 |
| NOV | 29.0 | 55.1 | 25.5 |
| DEC | 128.4 | 194.4 | 106.6 |
| JAN | 171.4 | 239.1 | 267.5 |
| FEB | 125.6 | 210.4 | 172.7 |
| MAR | 76.1 | 163.8 | 160.6 |
| APR | 10.1 | 41.1 | 36.7 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2025**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**


The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw


Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: